Mtendere umakhalapo mu mpingo ndipo Mulungu amasangalala pamene amuna ndi akazi onse amamutumikira mu ntchito imene anawarengera. Akazi sayenera kukhala akulu a mpingo, Atumiki, alaliki kapena atsogoleri a anthu popembedza Mulungu. Koma ntchito yawo yokhala amayi abwino ndi aphunzitsi a ana ndi akazi ena ndi yofunikaso. Tiyeni modzichepetsa tidzipereke ku chifuniro cha Mulungu.

.

FOR MORE INFO CONTACT;

rdgmissions@charter.net

www.icotb.org

MALO A LONGO MU MPINGO WA MULUNGU

Malo a amayi pakati pa anthu akukambidwa kwambiri masiku ano. Chikoka cha gulu la "kumasulidwa kwa akazi"(women's liberation) kapena feminist(chikazi) chimamveka pa dziko lonse la pansi. Amuna ndi akazi ambiri angavomereze kuti payenera kukhala kufanana pa ntchito ndi malipiro. Ambiri angavomerezenso kuti azikhala ndi ufulu ofanana ndi wa amuna. Komabe,amuna ndi akazi amene ndi akhiristu ayenera kutsutsa malingaliro ambiri a "gulu la chikazi"(Feminist movement) chifukwa amatsutsana ndi chifuniro cha Mulungu.

Mu mpingo wa Ambuye lero, Pali ena amene amafunsa za malo amene akazi ali. Ena akunena kuti akazi ali ndi ufulu wotsogolera mapemphero a pagulu, kulalikira ngakhaleso kukhala akulu a mpingo. Iwo akhala akusokeretsedwa ndi gulu la chikazi (Feminist movement) kapena mipingo ya mpatuko, makamaka achipentekoste,amene amalola akazi kuchita chilichonse chimene amuna amachita mu mpingo.

Akhristu amayenera kutsatira chifuniro cha Mulungu. Chifuniro cha Mulungu pa malo a akazi mu mpingo wake chaululidwa mu buku lake, Baibulo (2 Timoteo 3:16,17). Tiyenera kutsatira Baibulo ngati tikufuna kukondweretsa Mulungu ndi kupulumutsidwa kwa muyaya

Kodi Baibulo limati chiyani? Kodi udindo wa amayi mu mpingo ndi wotani?

Pali madera omwe amuna ndi akazi ali ofanana pamaso pa Mulungu. Chikondi cha Mulungu nchofanana kwa onse (Yohane 3:16). Mulungu alibe tsankho pa nkhani ya chipulumutso (Machitidwe 10:34,35). Amuna ndi akazi ayenera kutsatira dongosolo lofanana la chipulumutso ndipo adzalandira madalitso ofanana (Agalatiya 3:26-28). Komabe, pali madera amene dongosolo la Mulungu kwa akazi limasiyana ndi la amuna.

M'banja, Mulungu anaika mwamuna kukhala mutu(Aefeso 5:23). Mwamuna ayenera kupereka zosowa za kuthupi ndi zauzimu kwa mkazi ndi ana ake (Genesis 3:17-19; 1 Timoteo 5:8; Aefeso 6:4). Akazi ali ndi malo apadera mu dongosolo la Mulungu limene amuna alibe. Akazi ayenera akhale othandizira amuna awo,aphunzitsi a ana awo,ndi osamala pa nyumba (Genesis 3:16; Aefeso 5:22-23; Tito2:4,4). Amuna ndi akazi ndi osiyana thupi ndi kaganizidwe. Malo amene Mulungu adawaikira aliyese amawakomera monga momwe Mulungu adawapangira.

Pali malemba angapo amene amanena za udindo/malo a amayi mu mpingo. Mu 1 Akorinto 11:3, Mtumwi Paulo analeba ***"koma ndifuna kuti mudziwe,kuti mutu wa munthu yense ndiye Khristu; ndi mutu wamkazi ndiye mwamuna; ndipo mutu wa Khristu ndiye Mulungu.***" Mamuna ali ndi mutu umene ayenera kugonjera- Yesu Khristu. Mkazi alinso ndi mutu umene ayenera kugonjera- mwamuna. Koma ngakhale Khristu ali ndi mutu umene ayenera kugonjera- Mulungu Atate. Khristu sali wocheperapo kwa Mulungu chifukwa amadzipereka kwa Iye. Ndiponso mkazi sachepera kwa mwamuna chifukwa amagonjera mwamunayo. Malo amene Mulungu waikira amuna ndi akazi alibe chochita ndi kukhala ochepa mphamvu ndi otsogola. Zikugwirizana ndi cholinga chimene Mulungu anawalengera.

Timoteo woyamba,mutu wachiwiri, ndi ndime yofunikira kwambiri yomwe ikukamba za udindo wa akazi mu mpingo. Paulo akuyankhula za kupembedza kwapoyera kwa mpingo pamene iwo usonkhana pamodzi(1 Timoteo 2:1,2; 1 Timoteo 3:14,15). M'ndime yoyamba(vesi 1), Paulo akulamula kuti a zipempherera anthu onse. M'chinenero choyambirira cha chigiriki chimene Paulo analemba, liwu limene iye anagwiritsa ntchito ponena za munthu ndi "anthropos" limene liri lotanthauza anthu onse. Limaphatikizapo amuna ndi akazi omwe. Paulo akugwiritsanso ntchito mawu omwewa mu ndime ya chinayi(vesi 4) pamene akunena kuti, Mulungu.....***"amene afuna anthu onse apulumuke,nafike pozindikira choonadi."*** Koma mu ndime ya chisanu ndi chitatu(vesi 8), pamene Paulo akunena za kutsogolera m'mapemphero,akugwiritsa ntchito liwu losiyana kwa munthu. M'mawu achigiriki "aner". Mawuwa amagwiritsidwa ntchito ponena za amuna okha. Sichimaphatikizapo akazi! Lamulo, ndiye kuti amuna azitsogolera mapemphero apagulu a mpingo. Pali kusiyana koonekeratu pakati pa ndime ya chisanu ndi chitatu pamene akazi akulamuliridwa kuphunzira mwachete ndi kumvera konse. Mawu oti kumvera amachokera ku liwu lankhondo lachigiriki lomwe limatanthauza "kukhala wolamuliridwa." Mu ndime ya khumi ndi chiwiri (vesi 12), Paulo analemba: ***"koma sindilora ine kuti mkazi aphunzitse, kapena kulamulira mwamuna; komatu akhale chete***." akazi akuletsedwa ***" kukhala ndi ulamuliro"*** pa amuna. Sayenera kutenga mwayi umene suli wawo. Kulalikira ndi kuphunzitsa poyera m'makalsi amene amuna amakhalapo nzoletsedwa kwa akazi. Akazi akuletsedwa kutsogolera mwambo wa chipembedzo pamalo pamene pali amuna.

Paulo akupereka zifukwa ziwiri zomwe Mulungu anaperekera utsogoleri mu mpingo kwa amuna: (1). Adamu anayamba kulengedwa,kenako Heva (2) ndipo Adamu sananyengedwe,koma mkaziyo ponyengedwa analowa m'kulakwa. Mwamuna ali ndi utsogoleri pa mkazi chifukwa Mulungu anayamba kulenga iye poyamba. Mwamuna sanalengedwe kwa mkazi, koma mkazi kwa mwamuna (Genesis 2:8-15). Chachiwiri, Adamu sananyengedwe m'munda wa Edeni, koma Heva ananyengedwa (Genesis 3:16). Mkazi ndi wosiyana ndi mwamuna. Satana adatengerapo mwayi pa chikhalidwe chake chodalira kwambiri kuti amunyenge(amunamize). Adamu anachimwaso, koma sananyengedwe! anadziwa zimene anali kuchita ndipo mwadala analowa m'tchimo ndi Heva.

Akazi ali ndi mbali zambiri zodabwitsa za utumiki kwa Mulungu. Kubereka ana sitembelero limene linabweretsedwa chifukwa chakuti anachimwa mu Edeni, koma dalitso limene Mulungu anapatsa akazi pachiyambi (Genesis 1:28; Genesis 3:16). Akazi alinso ndi mwayi wa kukhala aphunzitsi, osati a amuna, koma kwa akazi amzawo ndi ana(2 Timoteo 1:5; Tito 2:3-5). Akazi achikhiristu ngati Priscilla,akhoza kuthandiza amuna awo kuphunzitsa ena mwamseri(Machitidwe 18:24-26). Akazi achikhiristu oopa Mulungu amaphunzitsa ena ndi chitsanzo chawo(1 Petro 3:12).